dziŵa kuti Mulungu ndi m'modzi, komanso ndi Anthu atatu.



## PHUNZIRO LA 3

1. Kodi palibe chiyambi, kunali mitsinje kapena nyanja, mapiri kapena mitengo?
-Iyayi.

2. Kodi palibe chiyambi, kunali nyama kapena mbalame, dziko la pasi kapena mlengalenga?
-Iyayi.

3. Kodi palibe chiyambi, kunali anthu oyera kapena akuda?
-Iyayi.

4. Kodi palibe chiyambi, kunali mizimu yiliyose?
-Iyayi.

5. Kodi ndi ndani Yekha amene analipo palibe chiyambi?
-Mulungu.

6. Chifukwa chakuti Mulungu yekha ndi amene analipo palibe chiyambi, kodi ndi ndani yekha amene angatiwuze ife za chiyambi?
-Mulungu.

7. Kodi Mulungu anayamba liti?
-Mulungu alibe chiyambi.
-Mulungu analipo chiyambire.
-Mulungu ndi wa nthaŵi zonse.
-Mulungu alibe mathero.

8. Kodi pali amene anamubereka Mulungu?
-Palibe.

9. Kodi Mulungu ndi amene anamubereka Mulungu?
-Iyayi.

10. Kodi pali amene anamulenga Mlungu?
-Palibe.

11. Kodi Mulungu anamulenga Mulungu?
-Iyayi.

12. Kodi pali nthaŵi imene kunalibe Mulungu?
-Palibe.

13. Anthu amafuna zakudya ndi madzi kuti akhale ndi moyo. Kodi Mulungu akusoŵa chiyani?
-Palibe. Mulungu sasoŵa china chilichonse kuti akhale ndi moyo.
14. Kodi Mulungu amakhala bwanji?
-Ndi mphamvu yake.

15. Kodi ndi ndani amene ali wamkulu kuposa dzuŵa, mwezi ndi nyenyezi?
-Mulungu.

16. Kodi ndi ndani amene ali wamkulu kuposa kumwamba ndi dziko la pansi?
-Mulungu.

17. Kodi ndi ndani amene ali wamkulu kuposa anthu onse?



kwa chakuti Iye amathamangathamanga.
-Iyayi.

-Buku la Mulungu silikuti Mulungu ali ndi thupi lalikulu kwambiri lokwanira pa dziko lonse la pansi.
-Iyayi.

-Buku la Mulungu silikuti Mulungu amamakhala pa dziko lonse la pansi.
-Iyayi.

-Buku la Mulungu likuti Mulungu ndi mzimu, ndipo amapezeka pena paliponse pa nthaŵi imodzi.

-Palibe amene angafanane ndi Mlungu.
-Mulungu ndi m'modzi ndipo amapezeka pena paliponse pa nthaŵi imodzi.

-Kaya tipite kuti, Mulungu ali komweko.
-Mulungu amatiwona nthaŵi zonse.

-Akutinso Mulungu ndi m'modzi m'buku lake.
-Mulungu ndi m'modzi komanso ndi Anthu atatu.

-Mulungu ndi Mulungu Atate.
-Mulungu ndi Mulungu Mpulumutsi.
-Mulungu ndi Mulungu Mzimu Woyera.

-Mulungu Atate, Mulungu Mpulumutsi ndi Mulungu Mzimu Woyera, ndi Mulungu m'modzi yemweyo.

-Pamene mudziphunzira zambiri za Mulungu, mudza-

-Kodi tikayesa kuti tibisale ku ntchire, titha kubisala kwa Mulungu?
-Iyayi.
-Sititha.

-Mulungu ali pena paliponse.

-Ife tingayese chotani kuti tibisale kwa Mulungu, sitingathe kuti tibisale kwa Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti Mulungu amapezeka pena paliponse pa nthaŵi imodzi.

-Kodi kutanthawuza kwake ndi chiyani tikati kuti Mulungu ndi mzimu?

-Apa pali chitsanzo:

-Kodi tingathe kuyiwona mphepo?
-Iyayi.
-Sitingathe.

-Kodi nanga kuli mphepo?
-Inde.

-Mulungu ndi mzimu.
-Ngakhale kuti sitikumuwona Mulungu, Iye ali pompano ndiponso ali pompo.

-Buku la Mulungu silikuti Mulungu ali palipose chifu-



-Mulungu.

18. Kodi ndi ndani amene ali wamkulu kuposa mizimu yonse?
-Mulungu.

19. Kodi chifukwa chiyani Mulungu ndi wamkulu kuposa china chilichonse?
-Chifukwa chakuti Mulungu yekha ndi amene analipo pachiyambi.

-Kodi chifukwa chiyani mukuganiza kuti Mulungu sakusoŵa chakudya ndi madzi?
-Chifukwa chakuti Mulungu alibe thupi ngati anthu.

-Kodi chifukwa chiyani mukuganiza kuti Mulungu sakusoŵa dzuŵa kuti adziwona ndipo dziko kuti adziyendapo?

-Chifukwa chakuti Mulungu alibe thupi.
-Chifukwa chakuti Mulungu alibe mafupa.
-Chifukwa chakuti Mulungu alibe magazi.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi mzimu.

-Kodi tsopano Mulungu ali kuti?
-Mulungu yekha ndi amene angathe kutiwuza ife za kumene Iye akukhala.

-Mulungu akuti ali palipose m’buku lake.
-Mulungu akuti ali palipose pa nthaŵi zonse.

-Mulungu ali kumwamba.
-Mulungu alinso pa dziko la pansi.

-Mulungu ali pompano tsopano lino.
-Mulungu ali palipose pa nthaŵi zonse.

-Mulungu ali ku Mangochi tsopano lino.
-Mulungu ali ku Monkeya Bay tsopano lino.
-Mulungu ali ku Blantyre tsopano lino.

-Mulungu amapezeka pena paliponse pa nthaŵi imodzi.

-Kodi zingatheke kuti munthu apezeke ku Mangochi ndi ku Blantyre pa nthaŵi imodzi?
-Iyayi
-Sizingatheke.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti munthu ali ndi thupi limodzi.
-Chifukwa chakuti munthu amatha kupezeka pa malo amodzi pa nthaŵi imodzi.

-Mulungu akupezeka pena paliponse pa nthaŵi imodzi chifukwa chakuti Iye alibe thupi.
-Mulungu akupezeka pena paliponse pa nthaŵi imodzi chifukwa chakuti Iye ndi mzimu.

-Mulungu akupezeka pena paliponse pa nthaŵi imodzi.

-Kodi mukaloŵa mnyumba mwanu , mumakhala ndi



ndani?
-Mulungu.

-Kodi mukapita ku munda kwanu, mumakhala ndi ndani?
-Mulungu.

-Kodi mukapita kukacheza kwa anzanu, mumakhala ndi ndani?
-Mulungu.

-Mulungu amapezeka pena palipose pa nthaŵi imodzi.

-Chifukwa chakuti Mulungu amapezeka pena paliponse pa nthaŵi imodzi, kodi tingathe kubisala kwa Mulungu?
-Iyayi.
-Sitingathe.

-Kodi tikayesa kuti tibisala pamwamba pa phiri, titha kubisala kwa Mulungu.
-Iyayi.
-Sititha.

-Mulungu ali pena paliponse.

-Kodi tikayesa kuti tibisale ku denga la nyumba, titha kubisala kwa Mulungu?
-Iyayi.
-Sititha.

-Mulungu ali pena paliponse.